

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

KODI WAMKULU KOPOSA ONSE NDANI?


(Nkhani yotsatirayi isonyeza zomwe mwina zimachitika pakati pa akuphunzira. Nkhaniyi yachokera m'mabuku awa: Luka 22:24-27; Marko 9:33-36; Mateyu 18:1-4.)

Pamene Yesu amayenda mu msewu wafumbi kuita ku Kapernaum, ophunzira anayenda pang'onopang'ono koteru kuti anatsalira m'mbuvo akukangana pamene amatsutsana kuti "kodi wamkulu ndani" (Marko 9:34b).

Iwo amayembekezera za kumasulidwa ku utsamunda wa ulamuliro wa Aroma ku dziko la Israyeli ndi Mesiya ngati mfumu ya mafumu. Akuphunzira sadazindikirebe kuti Ufumu wa Mulungu sunali wandale koma unali ufumu wa uzimu (Luka 17:21; Aroma 14:17).

Akuphunzira adakangana ndiponso adatsutsana kwambiri za amene amayenera kukhala ndi ulamuliro ndi ulema wambiri mu ufumu wa Mulungu. "Zoonadi ine ndine ndiyenera kukhala

wamkulu kuposa onse," adatero mmodzi. "Ndine wamkulu pakubadwa." "Iyai," wina adayankha. "Ine ndiyenera kukhala wamkulu chifukwa ndimadziwa kukhala ndi anthu-onani imvi zanga."



"Mukunama nonsenu," wina adatero mwaukali. "Ine ndine wophunzira kwambiri, wanzeru kwambiri ndiponso ndili ndi kuthekera kuposa awirinu."

"Chete," winanso adayankhula. "Ine ndakhala ndi Yesu kwa nthawi yaitali kuposa enanu. Ndine ndidali woyambirira kutsata Yesu."

Aliyense anayankhula mokweza

pakuteteza zomwe amayankhula. Zoonadi aliyense samafuna kuti wina awalamulire. Akutsutsana, wophunzira wina anayankhula motsitsa koma motsindika, "Ine ndidzakhala wamkulu kuposa onse. Banja langa ndi lolemekezeza m'dziko lonse la Israyeli."

Patapita nthawi, Yesu adafunsa akuphunzira ake, "Munalikutsutsana ninji panjira?" (Marko 9:33). "Kodi makamaka mulimbana za chiyani?" (Luka 22:24).

Yesu podziwa kudzikonda kwa mitima ya ophunzira anayamba kuwaphunzitsa za ukulu weniweni. Iye anaitana

kamwana pakati pavo nanena, "Chifukwa chache yense amene adzichepetsa yekha monga kamwana aka, yemweyo ali wopambana mu Ufumu wa Kumwamba" (Mateyu 18:4). "Ngati munthu afuna kukhala woyamba, akhale wakuthungo wa onse, ndi mtumiki wa onse" (Marko 9:35b).

"Mafumu a anthu a mitundu awachitira
(Yapitirira pa tsamba 2)

Zimene

BAIBULO

Limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyerera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba I)

ufumu;...Koma sipadzatero ndi inu; komatu iye ali wamkuru mwa inu, akhale ngati wamng'ono; ndi iye ali woyamba, akhale ngati wotumikira" (Luka 22:25-26).

Pakati pa anthu a Mulungu palibe kudzikonda. Pakati pa achipembedzo, abusa ambiri amafuna kukhala otchuka, amphanvu ndi odziwika. Iwo amafuna kukhala akulu kuposa ena pofuna kuti anthu aziwagonjera ndiponso kuwamvera. Amafuna kulamulira ngati mabwana ndiponso ngati mafumu mu mipingo komanso pakati pa abusa ena. Akhristu ambiri ndiponso abusa amayesetsa kuti anthu aziwapatsa ulemu ndiponso kuti akhale aulamuliro chifukwa chakuti ndi aakulu, amadziwa zambiri, maphunziro awo, mabanja kapena udindo wawo. Khristu adaphunzitsa ndiponso adaonetsa chitsanzo chosiyana ndi khalidwe lotere. Iye adaonetsa chitsanzo cha ukulu weniweni pa kudzichepetsa ndi pakutumikira.

Kodi wamkulu kuposa onse ndani? Wamkulu kuposa onse ndiye munthu amene amadzichepetsa ngati mwana wamng'ono, ndiye mwamuna kapena mkazi amene amatumikira anthu mwachikondi ndi kudzichepetsa mosadzikonda. Uku lu weniweni supezeka mu ulamuliro koma pakukhala ndi mtima wakutumikira ena. Mtima wotere sudzikweza koma umafuna kulemekeza ena. Tsongo mwana aliyense wa Mulungu komanso olalikira Uthenga Wabwino ayenera kupeza zoona za ukulu weniweni.

-mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choondi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyerera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gavo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choondi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu illiyonse molingana ndi chitsogozzo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.com. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choondi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zafulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

Mau a Mkonzi



Kutumikira Mulungu ndi mtima wodzichepetsa —Machitidwe 20:19a

Ndithokoza Mulungu chifukwa cha mwayi wodziwa oyera ndiponso nsanamira za mtchalitchi amene amandipatsa chitsanzo cha kudzichepetsa kwenikweni ndi utumiki kwa Mulungu. Tikukhala mu mbadwo wodzikonda komanso wonyada umene magwero a zolina ndi maloto a anthu ali pa kudzikonda. Khalidwe lotere lipezekango pakati pa anthu opembedza pamene abusa ndi odzikonda ndiponso ofuna kuti zonse zikhale za iwo wokha. Zimakhala zinthu zosakondweretsa kuona alaliki a Uthenga Wabwino kulakalaka maudindo a pamwamba, kudzikweza kwa umunthu, ndiponso kaduka ena akamachita bwino.

Komatu chimakhala chinthu chabwino kwambiri kuona atumiki a Mulungu odzichepetsa. Limakhala dalitso ku Mpingo wa Mulungu pakakhala anthu amene atsata modzichepetsa chitsanzo cha Ambuye wathu. Pakakhala kumenyana ndi mkangano, kawirikawiri pamakhalanso zodzikonda. Kudzichepetsa ndikofunika ndipo ndiumboni umene timafuna kuona tikamafuna kupeza atumiki enieni a uthenga wabwino.

M'gawo lino, taphunzira za lamulo la kusambsa mapazi ndi maphunziro omwe limatiphunzitsa. Chimakhala chinthu chodalitsika kukhala pakati pa anthu a Mulungu amene amakhulupirira ndi kutsata lamuloli, amene amadzichepetsa pa kutsukana mapazi. Kutsuka mapazi n'kosangalatsa ku thupi komatu ku uzimu kuli ndi mphoto zazikulu.

M'moyo mumakhala kusemphana maganizo komanso mavuto amene amabuka chifukwa chakusiyana makhalidwe komanso maganizo. Kudzichepetsa kudzathandiza kuthetsa mavuto onsewa amene anthu amakhala nawo ndi anzawo. Tsono pamafunika kudzichepetsa kuti munthu anene kuti "Ndinalakwa," kapena "Pepani." Ngakhale kuti tikutsata zolondola pa nkhanzi, nkofunika kwambiri kudzichepetsa mu mzymu. Mpingo kapena abale mwa Ambuye akakhala ndi mavuto, iyi ingakhale nthawi yabwino kusambsana mapazi ndi kupempha Mulungu kuti atipatse mtima wodzichepetsa kwambiri.

Munthu akakhala ndi chikhulupiriro kwambiri sindiko kuti alibe kudzichepetsa. Nthawi zambiri atsogoleri amanenedwa kuti ndiwodzikonda chifukwa cha ntchito imene amagwira. Tiyen'i tisamale kuti tisanene kuti anthu a Mulungu ndiwodzikonda chifukwa cha ntchito imene akugwira.

Ndikumbukira kalekale ndikuphunzitsa abusa za chitsanzo cha Khristu cha kudzichepetsa ndi kutumikira. Iwo sadakondwere nalo phunziroli chifukwa limatsutsa chikhumbokhumbo chawo chakuti utumiki wawo uwakweze ndikukhala pamwamba pa anthu. Izisizamachitike pakati pa anthu enieni a Mulungu. Cholinga chathu ndi maitanidwe athu ndizo kukhala ndi mtima komanso maganizo otumikira ndi kuyenda modzichepetsa.

Tiyen'i tifunefune Mulungu kuti tipeze ndi kuonetsa nthawi zonse mtima wodzichepetsa umene Yesu adafuna pamene amakhazikitsa lamulo la kutsuka mapazi.

Michael W. Smith

January 2015

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.us

kuti mudzilandira

makalata athu

kapenango kuti muone.



Inu Nonse Ndinu ABALE MWA AMBUYE

(Mateyu 23:1-12)

Afarisi amakonda
kukwezedwa komanso
kulemekezedwa ndi anthu.
Amalandira ulemu wa
maudindo awo. Yesu
anawalangiza
akuphunzirawo kuti
asamatchedwe Mphunzitsi,
Tate kapena Bwana. Khristu
ndiye bwana mmodzi ndipo
Mulungu ndiye tate wathu
mu uzimu kumwamba.

Ngakhale kuti alaliki
amakhala pa maudindo
osiyanasiyana m'thupi la
Khristu sayenera kutchedwa
maudindo (Tate, Mbeye,
Bishopu, Mbusa ndi mayina
ena).

Mpingo wa Chipangano
Chatsopano ulibe maudindo
osiyanasiyana a utumiki.
Koma atumiki onse
ndiwofanana. Monga Yesu
adanena, "Inu nonse ndinu
abale mwa Ambuye."

MLOZO WA KUSANTHULA BAIBULO

MUTU: MWAMBO WOSAMBITSA MAPAZI

Mawu a m'Baibulo: Chifukwa chache, ngati Ine Ambuye ndi Mphunzitsi, ndasambitsa mapazi anu, inunso moyenera kusambitsana mapazi wina ndi mnzache. – Yohane 13:14

Nkhani yonse mwachidule: Yesu Khristu adaika mwambo wosambitsa mapazi. Onse okhulupirira akuwalamula kutsatira chitsanzo ichi. Oyera a Mulungu amatchedwa ant-chito. Kusambitsa mapazi ndi chikumbutso chakuti onse ndi ofanana ndiponso chakudzichepetsa chimene chiyenera kukhala m'thupi la Khristu. (Werengani Yohane 13:1-17).

I. Unakhazikitsidwa ndi Khristu

Yohane 13:1-5 Yesu adasambitsa mapazi a akuphunzira.

II. Unalamulidwa ndi Khristu

- A. Mateyu 28:20 Tsatirani zinthu zonse.
- B. Yohane 13:14 Inu moyenera
 - 1. Muyenera: ngongole, womangidwa, kulamulidwa.
 - 2. Onani Luka 18:1;
Machitidwe 5:29; 1 Yohane 4:11

III. Khristu Anapereka Chitsanzo

Yohane 13:15 Chitsanzo cha Khristu.

IV. Unachitidwa ndi a Mpingo Woyamba

- A. Yohane 13:8 Chiyanjano ndi Khristu.
- B. 1 Timoteo 5:9-10 Akazi amasiye.

V. Phunziro la Kudzichepetsa

- A. Yohane 13:16 Kapolo sindiye wamkulu.
- B. Afilipi 2:3-7 Maganizo ngati a Khristu.
- C. Mateyu 18:1-4 Mukhale monga ana aang'ono.
- D. 1 Petro 5:3-5 Muvale kudzichepetsa.

VI. Kuitanidwa kukhala Atumiki

- A. Luka 22:24-27 Mfumu ngati wotumikira.
- B. Agalatiya 5:13 Tumikiranani wina ndi mnzake.

VII. Phunziro lakuti aliyense ndi wofanana ndi mzake

- A. Mateyu 23:8-12 Onse ali abale.
- B. Agalatiya 3:28 Amodzi mwa Khristu.

VIII. Madalitso kwa Omvera

- A. Yohane 13:17 Achimwemwe ndinu.
- B. Yesaya 1:19 Idyani zokoma za dziko.

Kumaliza: Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu, ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo...

—Afilipi 2:5-7



MWAMBO WA KUSAMBITSA MAPAZI

Nkhani yothandiza pa kusanthula Baibulo

ZOMWE BAIBULO LIMANENA

(Yohane 13:1-17) Yesu anaimirira nayang'ana akuphunzira amene adasonkhana. Adali atangomaliza kudya chakudya chamadzulo, chokumbukira Paska. Yesu adadziwa kuti kudatsala maola pang'ono kuti adzipereke ngati nsembe pa mtanda kuti apulumutse mtundu wa anthu. Chakudya ichi chotsiriza chidali pa nthawi ya mtengo wapatali pamene Khristu adakhazikitsa mwambo wolimbikitsa khalidwe lofunika kwambiri pa chikhaliidwe cha umulungu.

YESU ASAMBITSA MAPAZI A OPHUNZIRA

Ndimtima wachikondi, Yesu adaika pansi chovala Chake ndipo adadzimangirira ndi chopukutira. Adathira madzi m'beseni ndipo anagwada pamaso pa akuphunzira ake. Monga kapolo, anayamba kusambitsa mapazi awo ndipo anawapukuta ndi chopukutira chija. Atamaliza kusambitsa mapazi a ophunzira mmodzi, Yesu anafika pa Yudas.

Adamuyang'ana, pozindikira kuti padali patatsala pang'ono kuti Yudas amupereke iye. Mwachikondi komanso modzichepeta, Yesu anagwada patsogolo pa womperekaya kusambitsa mapazi ake.

PETRO ADZWONA KUTI NDI WOSAYENERA KUTI YESU ASAMBITSE MAPAZI AKE

Yesu atafika pomwe panali Petro, Petro adafunsa, "Ambuye, kodi Inu mundisambsita ine mapazi?"

Yesu adayankha kuti, "Chimene ndichita Ine suchidziwa tsopano; koma udzadziwa m'tsogolo mwache."

Petro podziona kuti sanali woyenera kuti Mwana wa Mulungu asambitse mapazi ake adayankha, "Simudzasambsita mapazi anga ku nthawi yonse."

Yesu adamuyankha nati, "Ngati sindikusambsita iwe ulibe cholandira pamodzi ndi Ine."

Petro anayankha mokhudzidwa nati, "Ambuye, si mapazi anga okha, komanso manja ndi mutu."

CHIZINDIKIRO CHAKUSAMBITSA MAPAZI

Atamaliza, Yesu adakhala pansi ndi ophunzira ndipo anayamba kufotokoza tanthauzo ndi kufunika kwa zimene anali atangochita. "Inu munditcha Ine Mphunzitsi, ndi Ambuye: ndipo munena bwino; pakuti ndine amene. Chifukwa chache, ngati Ine

Ambuye ndi Mphunzitsi, ndasambsita mapazi anu, inunso muyenera kusambsana mapazi wina ndi mnzache. Pakuti ndakupatsani inu chitsanzo, kuti, monga Ine ndakuchitirani inu, inunso muchite. Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Kapolo sali wamkulu ndi mbuye wache; kapena mtumwi sali wamkuru ndi womtuma iye"

(Yohane 13:13-16).

KUSAMBITSA MAPAZI SIMWAMBO WAMBA


Munthawi za m'Baibulo mwambo wosambsita mapazi umachitika

kawirikawiri chifukwa kunali fumbi. Idaali ntchito ya akapolo kusambsita mapazi a alendo. Yesu sadasambitse mapazi a ophunzira chifukwa cha fumbi. Yesu adali asanachitepo ichi n'kale lonse, monga taonera za khalidwe la Petro pa nkhanysi. Ichi chimene adachita Yesu chinali choposa mwambo wamasiku onse. Iye adauza Petro kuti, "Chimene ndichita Ine suchidziwa tsopano; koma udzadziwa m'tsogolo mwache" (Yohane 13:7). Yesu adakhazikitsa mchitidwe wosambsita mapazi ngati mwambo woti Mpingo uzitsata – mchitidwe umene umayimira komanso uli ndi tanthauzo la uzimu.

YESU ADALAMULIRA KUCHITA MWAMBO WOSAMBITSA MAPAZI

Yesu adatuma akuphunzira kupita kukalalikira ku maiko onse,

(Yapitirira pa tsamba 6)



*"Pakuti ndakupatsani inu chitsanzo,
kuti, monga Ine ndakuchitirani inu,
inunso muchite."*

(Kuchokera pa tsamba 5)

"ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu" (Mateyu 28:20). Yesu adaika malangizo omveka kuti anthu ake atsate mwambowu wosambitsa mapazi. Yesu ndiye adalamula kuti anthu azichita mwambowu. Yesu adati, "Inunso muyenera kusambitsana mapazi wina ndi mnzache." Mauwa m'Chigiriki atanthauza: kukhala ndi ngongole ndi wina, kumangidwa, kapena kukhala ndi udindo. "Anthu ayenera kupemphera nthawi zonse" (Luka 18:1b). "Tiyenera kumvera Mulungu kuposa anthu" (Machitidwe 5:29b). "Ifenso tiyenera kukondana wina ndi mnzache" (1 Yohane 4:11). Tsono apa tikuona kuti anthu a Mulungu ali ndi udindo wakusambitsa mapazi a ena. Komanso, Yesu adanena momveka kuti, "Pakuti ndakupatsani inu chitsanzo, kuti, monga lne ndakuchitirani inu, inunso muchite."

MPINGO UCHITA MWAMBO WOSAMBITSA MAPAZI

Ngakhale kuti mipingo yambiri imachita chikumbutso cha Mgonero wa Ambuye, komatu mipingo sichita chikumbutso chotsuka mapazi. Anthu ambiri safuna kutsukana mapazi ndipo amayesetsa kupeza chifukwa chomveka kuti asakhalepo pachikumbutsochi. Chikumbutso chakutsuka mapazi adachiphunzitsa Khristu koma chimachitika ndi mpingo woyamba. Mpingo umathandiza mkazi wamasiye ndi ndalamu "ngati adasambitsa mapazi a oyera mtima" (1 Timoteo 5:10). Anthu akamakana chikumbutsochi, akukana kudzichepetsa ndipo sakumvera malangizo a Khristu.

CHITSANZO CHA KUTUMIKIRA MODZICHEPETS

Yesu, Mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa ambuye adasonyeza kudzichepetsa ndi kutumikira kofunika ana enieni a Mulungu. Mpulumutsi adadzichepetsa osati kwa ophunzira okha amene adamukonda ndi kumutsatira, komanso kwa ophunzira amene adamupereka ndipo adali wachinyengo. Mzimu uwu wa Khristu ndiwosiyana kwambiri ndi mtima wolimbirana udindo ndi kutchuka umene upezeka pakati pa wopembedza a masiku ano. Anthu a Mulungu, abusa, atumiki, atsogoleri mu mpingo sali opambana Khristu. Chifukwa chaichi, pafunika kutsatira chitsanzo cha Khristu—osati ngati mbuye, mafumu koma ngati akapolo (Luka 22:25-27).

"MTIMA" WOSAMBITSA MAPAZI

"Musachite kanthu monga mwa chotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pache, komatu ndi kudzichepetsa mtima,



yense ayeze anzache omposa iye mwini; ...Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinsa mwa Khristu Yesu, ameneyo, ... anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo" (Afilipi 2:3-7). Kusambitsa mapazi a munthu wina ndi khaldidwe lodzichepetsa. Ichi ndicho chitsanzo cha mtima umene oyera ayenera kukhala nawo nthawi zonse. Akhristu muyenera kuti "mubvale kudzichepetsa kuti mutumikirane" (1 Petro 5:5). Ngakhale kuti mchitidwe wosambitsa mapazi sukutsatidwa tsiku lililonse, mtima wosambitsa mapazi uyenera kuti uzikhalapo m'moyo wa mkhristu.

PALI MADALITSO POTSATIRA MWAMBO WOSAMBITSA MAPAZI

Yesu adakhazikitsa mwambo wosambitsa mapazi kuti anthu AKE azikumbukira za mtima woona wa kudzichepetsa, kusadzikonda, otumikira ndiponso wosasankhana. Yesu amapereka mdalitso pa iwo omvera kutsatira chitsanzo chake m'thupi ndiponso mu mzimu. "Ngati mudziwa izi, odala inu ngati muzichita" (Yohane 13:17).

-mws



Kodi kusambitsana mapazi kuchitike kangati?

M'buku la Yohane 13 Yesu adaphunzitsa akuphunzira kuti ayenera kutsatira chitsanzo chake ndipo achite monga lye adachita pa iwo. Yesu sadapereke dongosolo lofotokoza kuti izi azizichita kangati. Lamulo ndicho chitsanzo cha chinthu cha uzimu. Kuchita ichi tsiku lililonse, sabata lililonse kapena mwezi uliwonse sicingakhalenso cha tanthauzo ndipo chingasanduke mwambo chabe.

Oyera mtima ambiri ali ndi lamulo lapadera la utumiki panthawi ya msonkhano wa pachaka. Mipingo ina ili ndi mchitidwe wosambitsa mapazi a oyera mtima pa nthawi imene Yesu amakumbukira Paska.

Yesu adasambitsa mapazi a Yesu panthawi ya Paska ndipo adachita Mgonero wa Ambuye. Iyi ndiyo nthawi yokumbukira imfa Yake ndi kukhomedwa pa mtanda. Chifukwa cha ichi, mwambo wosambitsa mapazi kawirikawiri amaukumbukira pa chipembedzo chomwecho chimene akhale akulandira Mgonero wa Ambuye. Chofunika kwambiri si kuchuluka kwa nthawi imene izi zikuchitika koma mmene zikuyenera kuchitikira.

Kodi n'koyenera kuti amuna ndi akazi azisambitsana mapazi?

Malembo akunena pa Luka 7:37-39 za mkazi amene adasambitsa mapazi a Yesu ndi misozi yake. Ngakhale kuti anthu amene amadziyesa oyera, ichi chidali chinthu chapadera chidasonyeza kupemphera ndiponso ulemu kwa Ambuye Yesu. Ichi sichidali chinthu chimene mayi uja adayambitsa kuti ena atengerekro nkumachita mtsogolo.

Pali ulemu pakati pa amuna ndi akazi umene sichanzeru kuuphwanya kaamba ka mchitidwe wa chipembedzo wa kusambitsa mapazi. Pali miyambo ina pakati pa anthu ena kumene mkazi wa panyumba amasambitsa mapazi a

awa ndiwoyenera kwambiri.

Ndibwino komanso ndikoyenera kuti a amuna ndi a akazi achite ichi paderapadera. Amuna asambitse mapazi aamuna ndiponso kuti akazi asambitse mapazi aakazi anzawo.

Kodi pakusambitsa mapazi kodi munthu aliyense asambitse mapazi a aliyense amene ali pamalopo?

Pakupereka chitsanzo, Yesu adasambitsa mapazi a ophunzira onse. Kenaka adawauza kuti "inunso muyenera kusambitsana mapazi wina ndi mnzache" (Yohane 13:14b). Kukadakhala kosatheka kwa munthu mmodzi kusambitsa mapazi a aliyense pa gulu lalikulu. Chofunika kwambiri pa mchitidwe wosambitsa wa umunthu komanso wa uzimu ndi kudzichepetsa pa kugwada pansi ndi



mlendo wolemekezeka onse apabanja alipo. Mwambo wotere ufananako ndi zomwe zidamuchitikira Khristu. Mwambo wotere sufanana ndi chikumbutso cha kusambitsa mapazi a anthu oyera.

Ngakhale kuti samayankhula za nkhaniyi, buku la, 1 Akorinto 14:40 likuti, "Koma zonse zichtike koyenera ndi kolongosoka." Mawu

kusambitsa mapazi a munthu wina.

Ngati munthu mmodzi asamBITSA mapazi a minthu wina, ndipo munthuyu asamBITSA mapazi a munthu wina, ndipo onse akachita ichi aliyense adzasamBITSA ndiponso adzasamBITSidwa. Potero, iwo "asamBITSANA mapazi wina ndi mnzache."


-mws



KODI MUKUDZIWA?

Umboni usonyeza kuti pali Akhristu amene amachita khalidwe lakutsuka mapazi kuyambira kalekale. Mfumu Augustine (A.D. 400) adavomereza mwambowu. Mwambowu udatchuka kwambiri kalekale ku Ulaya cha kummwera. Anthu Obatizanso (Anabaptists) amatsata chipunzitsochi m'zaka za 1600.

Mipingo ya chiBaptist ya ku America imatsata mchitidwe wakutsuka mapazi m'zaka za 1900. Abraham Lincoln, ali mnyamata, adakonza madzi ndi mabeseni pa mwambo wake m'tchalitchi cha Baptist cha kummwera kwa dera la Indiana ku America.
[Brown, Charles E. (1947). *The Apostolic Church.*]



Wotumikira Khristu

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.com

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Paulo, mtumiki wa Yesu Khristu adaitanidwa kukhala ophunzira, wopatulidwa mwa mawu a Mulungu. —Aroma 1:1

Atumiki enieni amaitanidwa ndi kudzozedwa ndi Mulungu. Amasankhidwa kulalikira uthenga ndi kuyankhula monga momwe mzimu wawalankhulitsira. Paulo adadzitcha "kapolo wa Yesu Khristu." Iye amadziwa kudziwa Khristu ngati Mbuye. Iye sadadzitengere ulamuliro wa iye yekha koma adatumikira ndiponso adayankhula monga wantchito kuchita chifuniro cha mbuye wake.

Pamene kapolo akumvera malamulo, mbuye ndiye amalandila ulemu. Pamene Mulungu adalitsa ndi kudzoza ntchito za mtumiki mu Ufumu wake, ulemu ndi matamando zimapita kwa Ambuye. Mtumiki amene ali ndi umulungu asakwezedwe chifukwa cha kuthekera kwake kapena mwa ntchito zake popeza onse ndi akapolo.



Nthawi zina atumiki amagwa ulesi akaona kuti ntchito zaho sizikubala zipatso zambiri. Nthawi zina mapemphero sayankhidwa. Atumiki amasenza mtolo uwu ndipo ungawalemere chifukwa chakulephera kukhala ndi kuthekera kopangitsa kuti zinthu ndiponso anthu asinthe. Limbani mtima ndipo kumbukirani kuti inu ndinu kapolo chabe. Ndimphamu ya Mulungu komanso ndi chifuniro cha Mulungu chimene chingonetse zotsatira pa nthawi yake komanso mwanjira yake. Mukhale wogonjera, womvera, ndi wokhulupirika ndipo zotsatira zonse muzisiye m'manja mwa Ambuye. Kwezani mitu yanu kumwamba ndipo kwanirtsani cholinga cha Mulungu modzichepetsa monga mtumiki wa Yesu Khristu.

—mws